

CHIPILIRO CHA WOYERA MTIMA

Updated 20/9/08

Iwo wokhulupilira chipunzitso cha chiterezo cha muyaya (Ukapulumutsidwa kamodzi kwakwana) amanena kuti ngati munthu wapulumutsidwa, sikungatheke munjira ina iri yonse kutaya chipulumutso chake. Kunena kuti, ndiotetezedwa kwa muyaya chifukwa machimo ake onse, akale komanso amtsogolo, akhululukidwa. Iwo amati, ukapulumutsidwa, ngakhale utayenda moyo wa uchimo, sungataye chipulumutso chako, koma ungataye chiyajano ndi Yesu Khristu basi. Saverengera mawu opezeke pa **Aheberi 12:14** omwe akuti: "*Londolani mtendere ndi anthu onse, ndi chiyeretso chimene, akapanda ichi, palibe m, modzi adzaona Ambuye*". Chipunzitso chopulumutsidwa kamodzi chikupangitsa chiyero chopanda phindu koma chongoonjezerapo.

Ma vesi otsatirawa, akutsutsana ndi chipunzitsochi:

Mateyu 7:21 Yesu akuti okhawo akuchita chifuniro cha Atate ake, adzalowa mu ufumu wa Kumwamba. Chifuniro cha Mulungu ndi chain? **1 Atesalonika 4:3** akutiuza kuti "pakuti ichi ndi chifuniro cha Mulungu, chiyeretso chanu". Ndipo **2 Atesalonika 2:13** ikulumikizitsa chipulumutso ku kukhulupirira **ndi** kuyeretsedwa pamene mawu akunena kuti: "*Mulungu anakusankhani inu kuyambira pachiyambi mulandire chipulumutso mwa chiyeretso cha Mzimu ndi chikhulupiriro cha choonadi*." Zitsanzo zotsatirazi zikutionetsa momveka bwino kuti wokhulupirira angatye kutaya chipulumutso chake.

MAWU WONENA KUTI 'NGATI'

Yesu Khristu anabweretsa kwa ife chipangano chatsopano ndipo monga zipangano zonse, pali mfundo zoyenera kutsatiridwa kuti phindu likalandiridwe. Mu chipangano chatsopano mawu wonena kuti 'ngati' agwiritsidwa ntchito mochulukira pogwirizana ndi chipulumutso. Pamene Mulungu wakhazikitsa mfundo zogwirizana ndi mawu oti 'ngati', ndipo anthu sakutsatira mfundozi, ndikosatheka kuona zotsatira kapena kuti phinda chifukwa Mulungu samalankhula popanda pake.

Aroma 8:12-14 akunena momveka kuti akhristu ali a mangawa kusakhala moyo wa uchimo kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyer, kupanda kutero, tidzafa. "...*chifukwa chake abale, tiri amangawa si ake athupi ayi kukhala ndi moyo monga mwa thupi, pakuti ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi, mudzafa: koma ngati ndi Mzimu mufetsa zochita zake za thupi, mudzakhala ndi moyo...*" Yesu akunena momveka kuti kumvera ndicho cholowa cha chipulumutso. Pa **Yohane 15:10** Yesu akuti: "*Ngati musunga malamulo anga mudzakhala mchikondi changa...*" Ngati sitimvera chitsogozo cha Mzimu, sitikhala m'chikondi cha Mulungu koma tidzadulidwa mu mpesa monga mawu akunena pa **Yohane 15:6**.

Ena amati mawu wonena kuti 'ngati' satanthauza 'ngati' nthawi zonse, nthawi zina amatanthauza 'popeza'. Tikayika 'popeza' m,malo mwa 'ngati': **Aroma 8:13** ananena kuti: '**popeza**' mukhala ndi moyo monga mwa **thupi, mudzafa, koma 'popeza'** ndi Mzimu mufetsa zochita zake za thupi, **mudzakhala ndi moyo**'. Tanthauzo la vesili lasinthika.

Aheberi 10:38 ananena kuti: '*koma wolungama wangayo adzakhala ndi moyo wochokera mchikhulupiriro: ndipo 'popeza' abwerera, moyo wanga ulibe kukondwera mwa iye.*'

Ndi 'ngati' yekha yemwe akupereka tanthauzo lomveka pa zitsanzo ziwirizi. Ndipo ma vesi onse awiriwa, akutsutsana ndi chiterezo cha muyaya kwa okhulupirira.

KAPOLO WOKHULUPIRIKA NDI WA NZERU - LUKA 12:42-46

Chonde werengani **Luka 12:42-46** ndipo muona kuti pali woyang'anira wokhulupirika ndi wa nzeru m'modzi yekha basi.

Tikayang'anitsitsa vesili:

V.42 – Woyang'anira wokhulupirika ndi wa nzeru waikidwa kukhala kapitawo pomwe mbuye wake wachokapo.

V. 43-44 – Ngati Mbuye wake pobwera adzapeza kut anali okhulupirika, adzamuika kukhala kapitawo wa pa zonse ali nazo.

V. 45-46 – Kapolo yemweyu, adzayikidwa pamodzi ndi wosakhulupirira ngati mbuye wake pobwera ampeza wagwa mu uchimo komanso kuzunza akapolo anzake.

Pamene mawu akunena kuti kapolo ameneyo azaikidwa pamodzi ndi wosakhulupirira, zitanthauza kuti: poyamba anali wokhulupirira. Izi zikuonetsa poyera kuti munthu wopulumutsidwa akhoza kutaya chipulumutso chake.

MPESA NDI NTHAMBI ZAKE - YOHANE 15

Pa Paska omaliza, **Yohane 15:1-6**, Yudasi anachokapo ndipo Yesu anali kulankhula ndi ophunzira khumi ndi m'modzi ndi wotsalawo, ndikuwatchula kuti Nthambi. Tikaonetsetsa ma vesi amenewa, tikuona kuti:
V.1 – Mpesa umodzi wokha watchulidwa – ndiye Yesu ndipo Mulungu ndiye mwina munda.
V.2-3 – Mulungu adula nthambi iri yonse yosabala chipatso ndipo nthambi yakubala chipatso ayisadza.
Vs.4-5 – Nthambi (ophunzira) akuuzidwa kukhala mu mpesa kuti abereke chipatso.
V.6 – Nthambi yosakhala mu mpesa ayitaya kunja, ifota, ayisonkhanitsa, nayitaya kumoto.
Ndi opulumutsidwa okha omwe angakhale nthambi mu mpesa ndipo mu fanizoli, tikuona kuti moyo wopulumutsidwa ukhoza kudulidwa kuchoka mu mpesa ndi kukathera ku moto – Gehena.

KUYANJANITSIDWA, KUYERETSEDWA NDI KUKHALA MU CHISOMO

Ngati munthu wayanjanitsidwa, wayeretsedwa ndipo akukhala mu chisomo, izi zikutanthauza kuti ndi opulumutsidwa. Ma vesi otsatirawa akupereka zitsanzo za anthu omwe anali opulumutsidwa koma akhoza kukumana ndi chiweruzo chifukwa cha tchimo.

Kuyanjanitsidwa: **Akolose 1:21-23** akuti, "*ndipo inu okhala alendo kale ndi adani mchifuwa chanu m'ntchito zoipazo, koma tsopano anakuyanjanitsani m'thupi lake mwa imfayo, kukaimika inu oyera ndi opanda chirema ndi osatsutsika pamaso pake ngatitu mukhalabe m'chikhulupiriro*" Apa, tikuuzidwa za omwe anali adani a Mulungu omwe tsopano ayanjanitsidwa, abadwa mwatsopano, ndipo azaonetsedwa kwa Mulungu **pokhapokha** akaima mu chikhulupiriro. Anthu amenewa, ndiopulumutsidwa ndithu. Chibvomerezo chabodza, sicingatiyanjanitse ndi Ambuye. Pamene tayanjanitsidwa, tikuyenera kuimabe mu chikhulupiriro chathu kuti tikafike kumwamba.

Kuyertsedwa: **Aheberi 10:26-29** akuti "*Pakuti tikachimwa ife eni ake, titatha kulandira chidziwitso cha choonadi, siitsalanso nsembe ya kwa machimo, koma kulindira kwina koopsa kwa chiweruzo ndi kutentha kwake kwa moto ... munthu woeputsa chilamulo cha Mose angofa popanda ... nayesa mwazi wa chipangano umene anayeretsedwa nao*" Pa mavesi amenewa, tikuona kuti munthu wopulumutsidwa (woyeretsedwa ndi mwazi) adzaweruzidwa ngati apitiliza kuchimwa mwadala. Ngati okhulupirira alephera kulapa tchimo, mtima wake udzalephera kutsutsika ndi Mzimu. Patapita nthawi, zizakhala zovuta kulapa ndipo wokhulupirira angathe kutaya chipulumutso chake - **Aheberi 3:7-14**.

Mwa Chisomo: **Agalatiya 5:4** akuti "*Mulibe kanthu ndi Khristu, inu amene muyesedwa olungama ndi lamulo, mudagwa posiyana nacho chisomo.*" Ayuda awa, atasiyana nacho chilamulo cha Mose, alekanitsidwa ndi Ambuye, asiyana nacho chisomo. Mwachidziwikire, poyamba anali mu chisomo, kunena kuti anali wopulumutsidwa.

MA VESI ENA OTSATIRA

Yakobo 5:19-20 akuti, "*Abale anga, ngati wina wa inu asochera posiyana nacho choonadi, ndipo ambwenza iye mzache, azindikire kuti iye amene abweza ochimwa ku njira yake yosochera, adzapulumutsa munthu kwa imfa, ndipo adzabvundikira machimo aunyinji.*" Abale a chikhristu akulimbikitsidwa kubwenza abale awo wosochera ndi cholinga chowapulumutsa ku Gehena.

1 Timoteo 4:16 akuti, "*Udzipenyerere wekha ndi chiphunzitsocho, uzikhala mu izi, pakuti pochita ichi udzapulumutsa iwe wekha ndi iwo akumva iwe.*" Mwachidziwikire, Timoteyo akadapanda kupirira, akadataya chipulumutso.

CHIPILIRO NDI CHIYANI?

Pali kusiyana pakati pa tchimo longobwera komanso tchimo lochita dala. **1 Yohane 2:1** akutiua kuti m'khristu akhoza kuchimwa mwa nthawi, ndipo tchimo ili liunikiridwe monga m'mene **1 Yohane 1:9** akunenera:... wochimwa akavomereza amakhululukidwa komabe, kukhala moyo wochimwa mwadala, kungaononge chipulumutso chako. Wokhulupilira ena amavutika ndi tchimo, mwina kwa nthawi yaitali, koma, kuvutika ndi tchimoku kukusonyeza kuti ali ndi mtima wofuna kulapa, ndipo Mulungu adzawamasula mu nthawi yake. Izi zikusiyana ndi kukhala moyo wa uchimo; ndikumanena kuti "Ine ndikukhala kwanga, ndine wathupi la nyama." Mphotho ya uchimo (wosavomerezewa) ndi mfa.

Si chipulumutso cha ntchito, kuti munthu apulumutsidwe, akuyenera kukhulupirira ndi kulapa machimo, ndipo izi sizikutanhtauza ntchito – ndi chifuniro cha *mkati* mwa mtima. Chipiriro chikutanthauza kuvomereza, kulapa, ndi kukhulupirira mwa Yesu. Ngati chipiriro chiri mu ntchito; zitanthauza kuti chivomerezo ndi kulapa kwathu kukadakhala kudzera mu ntchito; koma siziri choncho. Baibulo likupitiriza kutipempha kuti tilape machimo athu onse ndikuyenda mu Mzimu kuti tikhalebe mwa Yesu. Timapulumutsidwa pamene tikhalabe mwa Khristu (**Yohane 15:1-6**). Mzimu wa Mulungu amagwira ntchito m'katu mwathu kutitsutsa, kutipangitsa kulapa komanso kutipatsa mphamvu yokana tchimo. Kuti tikayende mu chiyero, tikuyenera kusankha chipiriro ndikukhala mwa Yesu. (**Yohane 6:28-29**)

Aroma 8:35-39 akuti palibe cholengedwa chomwe chingatilekanitse ndi chikondi cha Mulungu; kapena njala, kapena lupanga, angelo kapena ziwanda. Zinthu zonsezi ndi *zakunja* ndipo sitingathe kuzilamulira. Mulungu akulonjeza kutipyoletsa m'mayesero onsewa monga mawu akunenera pa **Aheberi 13:5-6**. Komabe, ma vesi amenewa sakulankhula za chipiliro cha m'katu chomwe chimafunikira kuti tikayende moyo wa chiyero mwa Mzimu. Tiri ndi ufulu kuchita izi. Mulungu samalamulira chifuniro chathu. Iye amatilola kuchita monga mwa kufuna kwake kwabwino **Phil 2:13**.

CHOMALIZIRA

Mawu woti 'ngati' mu ma vesi ochuluka komanso mmene afotokozeredwa pa **Yohane 15:1-6** komanso **Luka 12:42-46** akuyenera kuti tiwamvetsetse. Monga mtundu wa Israyeli, kumvera kumafunika kuti mukakolole phindu la malonjezano monga kwalembedwa pa **Yesaya 1:19-20**. Wonani langizo kwa woyeria mtima pa mawu opezeke pa **Ezekiel 3:12-13**. Tinapulumutsidwa mwa chisomo kudzera mu chikhulupiriro ndipo kuti tikakhale opulumutsidwabe, tikuyenera kuperira mu chikhulupiriro komanso wosakhala moyo wochimwa dala, kukhalabe mu uchimo kapena kuhala ndi tsogolo lopanda Khristu. Palibe yemwe angakhale moyo wosachita tchimo. Tonse timachimwa nthawi zina koma tizalangidwa ngati tipitilira kuchimwa mwadala. **1 Yohane 2:1-2** akuti wokhulupirira asachimwe koma tikachimwa, tikuyenera kubwera kwa Yesu molapa, ndipo azitikhululukira ndikutiyeretsa monga kwalembedwa pa **1 Yohane 1:9**. Mawu onena kuti 'ngati' mu vesili ndiofunikira kwambiri Ngati sitivomereza, sitidzakhululukidwa. Chisankho chiri ndi ife eni. Ngati inu mukuwerenga buku ili, kodi munamufunsa Yesu kuti akupulumutsensi? Koma ngati muli ndi machimo omwe simunawavomereze, chonde gwadani pansi ndipo mufike pamaso pa Mulungu ndi kulapa. Amakukondani ndipo akuyembekezera kuti akuyeretseni mu chisalungamo chonse.

Yesu anati: "...koma iye wakupirira kufikira chimaliziro, yemweyo adzapulumutsidwa." **Mark 13:13**

Pali ma vesi ochuluka omwe angatsutsane ndi chiphunzitso cha kupulumuka kwa tuyaya koma buku ili langotifotokozerwa modula. Buku lina lomwe linalembedwa ndi Robert Shank lotchedwa 'Moyo uli mwa Mwana', likufotokozerwa mwakuya kuti chiphunzitso cha kupulumuka kwa tuyaya ndi chiphunzitso chabodza. Pachiyambi Robert Shank anali kukhulupirira kwathunthu pa chiphunzitso chakupulumuka kwa tuyaya, koma anasinthika. Sipakusowekanso kuhala ndi nzeru ya chi Greek kuti tione kufunikira kwa u Mulungu koti wokhulupirira akuyenera kuperira kuti akalandire moyo wosatha.

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

Written by:
Mick Alexander
Email: leeandmick@gmail.com
www.ChristianIssues.biz